# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA RUMPHI M'DZINJA LA 2024-2025

## DZINJA LA 2024/2025 MWACHIDULE


Nyengo ya dzinja ya 2024/2025 ikuyembekezeka kukhudzidwa ndi LaNina. La Nina ndi kuzizira koposera mlingo kwa madzi pakati cha kum'mawa kwa nyanja ya mchere ya Pacific.
Madera ambiri m'bomali akuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo okhazikika kapena kuposera mlingo okhazikika. Ngakhale zili chonchi, mvula idzachepera mlingo okhazikika mu mwezi wa November.

## October 2024





October ndi mwezi umene nthawi zambiri kumakhala nyengo yotentha komanso kopanda mvula. Komabe, Ulosi ukuonetsa kuti m'madera ena adzalandira mvula ya Chizimalupysa

## November 2024





Madera ambiri kudzakhala nyengo yotentha, mphepo ya mkuntho, Ziphaliwali ndi mabingu. Mvula ya mabingu ikuyemebkezereka kudzagwa m'madera ena ochepa yomwe mulingo wake udzafike 50mm

## December 2024





Mwezi wa December, madera ambiri adzalandira mvula, yomwe idzakhale ya mlingo wa pakati pa 150mm ndi 200mm. Mvula yoposera mlinog wa 200mm idzagwa m'madera monga Nyika Plateau ndi SC Mwalweni Mvula yodzalira ikuyembekezereka sabata yachiwiri mweziwu

## January 2025





M'mwezi wa January, madera ambiri adzalandira mvula yoposera 250mm. Madera monga SC Mwahenga ndi Mwankhunikira adzalandira mlingo wapakati pa 150mm ndi 200mm

## February 2025





Areas around East of Nyika Plateau and SC Mwalweni are forecast to receive more than 200mm.
Mvula idzapitilira m'mwezi wa February, ndipo madera ambiri akuyembekezereka kuti adzalandira mlingo wa pakati pa 100mm ndi 150mm. Madera ena monga ku Nyika ndi SC Mwalweni akuyembekezera kudzalandira mvula yoposera 200mm

## March 2025




Mvula ya mlingo okhazikika ikuyembekezeka mwezi wa March. Madera ambiri adzalandira mvula ya mlingo wa pakati pa 150mm ndi 200mm. Madera ena monga TA Zolokore, SC Mwalweni ndi Kachulu adzalandira mvula ya mlingo oposera madera ena onse a m'bomali


## April 2025




Madera ambiri akuyembekezera kulandira mvula ya mlingo wa pakati pa 50mm ndi 100mm. Madera okwera aku Nyika adzalandira mvula yochuluka kuposera mlingowu. Dzinja likuyembekezeka kufika kumapeto sabata ya chitatu ya mwezi wa April m'madera ambiri.

- Mvula yodzalira idzachedwerapo, ndipo ikuyembekezeka pakati pa sabata ya chitatu ndi yachinayi mwezi wa December 2024.
- Dzinja likuyembekezeka kufika kumapeto sabata ya chitatu ya mwezi wa April m'madera ambiri.
- Dzinja likuyembekezeka kukhala yotalika masiku 90 ndi 100.
- Ng'amba ya ma sabata awiri ikuyembekezeka mu January, ndipo ya sabata imodzi mu February

| RUMPHI | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 0.0 | 6.1 | 9.6 |
| NOV | 22.4 | 65.5 | 13.1 |
| DEC | 132.8 | 215.4 | 181.0 |
| JAN | 183.8 | 242.7 | 248.6 |
| FEB | 152.6 | 203.6 | 205.9 |
| MAR | 104.6 | 179.0 | 196.6 |
| APR | 24.5 | 55.8 | 95.9 |




**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2024**

**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**
The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw

Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku: